UNDUNA WA ZACHILENGEDWE

NTHAMBI YOWONA ZANYENGO NDI KUSINTHA KWA NYENGO

# NYENGO MSABATAYI

## KUYAMBIRA PA 27 APRIL MPAKA PA 3 MAY 2026


## NYENGO M'SABATA IKUBWERAYI

Kuyambira mawa mpaka Lachiwiri pa 28 April 2026, tiyembekezere nyengo ya mitambo yapatalipatali, ya chifunga ndi mvula m'madera ochepa makamaka a mphepete mwanyanja a m'chigawo chakumpoto.

Ndipo mvula yowaza/yamawawa idzafalikira m'madera a mchigawo chapakati ndi kummwera kuyambira Lachitatu pa 29 April mpaka Lachinayi pa 30 April 2026. Komanso kudzakhala nyengo ya mphepo, mitambo ndi chifunga.

Koma kuyambira Lachisanu pa 1 May 2026 mpaka kumapeto kwa sabatayi, tiyembekezere nyengo ya mphepo, ya mitambo yapatalipatali ndiyofunda ndi mvula m'madera ochepa makamaka amphepete mwanyanja kumpoto kwa dziko lino.

**Mphepo ya mwera ikuyembekezereka kuomba pa Nyanja.**




*Ulosi wamvula kuphatikiza masiku onse musabatayi.*

## NYENGO MU SABATA YANGOTHAYI

Msabata yapitayi, kunali nyengo ya mphepo, mitambo ndi yofunda m'madera ambiri komanso mvula m'madera ochepa makamaka akumpoto m'phepete mwa nyanja.

Mvula yambiri m'maola 24 yomwe tinalandira inali ya mlingo wa **31.1mm kuchokera ku Kambenene station ku Karonga pa 22nd April, 2026.**

## LANGIZO:

**Mphepo ya mphamvu pa nyanja:** ogwiritsa ntchito Nyanja akhale osamala.

***For further information please contact:*** *The Director, Department of Climate Change and Meteorological Services, Ministry of Natural Resources and Climate Change, P. O. Box 1808, Blantyre, Malawi. Tel: (265) 882 266 579; Email: metdept@metmalawi.gov.mw , Website: www.metmalawi.gov.mw*

**Malo osindikizira: Blantyre**

**Yatsindikizidwa Lamulungu pa 26 April, 2026.**